

KUTHANDIZA AZIMAYI KUM'MWERA KWA AFRIKA KUCHITA BWINO PA BIZINESI

**Buku lofotokoza mfundo zothandiza
azimayi amene amagula ndi
kugulitsa zinthu kunja**

Kuthandiza azimayi kuti akhale odziimira
pankhani yodziwa bwino malamulo onse
okhudza ziyeneretso zochitira bizinesi
m'mayiko a kum'mwera kwa Africa.



Mawu Oyamba

Mabizinesi ang'onoang'ono okhudza kugula kapena kugulitsa zinthu m'mayiko ena amathandiza kwambiri pa ntchito yochepetsa umphawi ndiponso njala. Mabizinesi amenewa akuthandiza ndithu pa chitukuko cha mayiko osauka a kum'mwera kwa Africa. Ndalama zobwera chifukwa cha mazibinesi amenewa n'zofunika kwambiri pa ntchito yochepetsa umphawi.

Ambiri mwa amene amachita bizinesi zoterezi ndi azimayi. Ofufuza apeza kuti m'mayiko omwe ali mbali ya Southern Africa Development Community (SADC) pa anthu 100 aliwonse ochita bizinesi zomapita m'mayiko ena 70 ndi azimayi. Pochita bizinesi zoterezi azimayi amakumana ndi zambiri poyerekezera ndi azibambo.

Ena mwa mavuto amene amakumana nawo ndi monga; kusakhala ndi njira zabwino zowathandiza kudziwa komanso kumvetsa malamulo okhudza misonkho ndiponso ndondomeko ya mafomu a pa boda, kusakhala ndi chitetezo chokwanira pa boda kwa azimayi ndi ana komanso kusowekera kwa zipatala ndi zimbuzi zabwino m'maboda.

Cholinga cha buku lino ndicho kuthandizapo pa limodzi mwa mavuto amenewa, pofotokoza zimene azimayiwa akuyenera kudziwa zokhudza ndondomeko ya mafomu m'maboda. Buku lino likufotokoza mbali izi; dongosolo lounika zinthu zomwe zimabwezera m'mbuyo abizinesi owoloka boda (non-tariff barrier reporting system), dongosolo la mu mgwirizano wofewetsa nkhani za malonda pakati pa maiko a kum'mawa ndi kum'mwera kwa Africa (Common Market for Eastern and Southern Africa (COMESA) Simplified Trade Regime), mndondomeko wa katundu wodziwika bwino (common list of goods), mfundo za mu mgwirizano wa zamalonda wa mayiko a mu SADC (SADC Free Trade Area) ndi mfundo zochirikiza ufulu wa amayi a bizinesi (the voice of women traders).



Ntchito yokonza bukuli yachitidwa ndi a Southern Africa Trust and Southern Africa Cross Border Traders Association ndi thandizo OSISA

www.southernafricantrust.org; www.sacbta.org;

ZAMKATIMU

PEJI

1. COMESA SIMPLIFIED TRADE REGIME (STR)	4
2. Kodi COMESA STR ndi chiyani kwenikweni?	5
3. Kodi muli ndi ziyeneretso zogwiritsa ntchitoZVINOITWA	6
4. Kulwetsa kapena kutulutsa katunda pogwiritsa ntchito dongosolo la COMESA STR	10
5. Gulu 1: STR COMMON LIST (Katundu Wovomezedwa): Ku Zambia ndi ku Malawi	12
6. Gulu 2: STR COMMON LIST (Katundu Wovomezedwa): Ku Zambia ndi ku Zimbabwe	15
7. Gulu 3: STR COMMON LIST (Katundu Wovomezedwa): Ku Zimbabwe ndi ku Malawi	20
8. Gulu 4: STR COMMON LIST (Katundu Wovomezedwa): Ku Malawi ndi ku Zambia	22
9. Gulu 5: STR COMMON LIST (Katundu Wovomezedwa): Ku Malawi ndi ku Zimbabwe	24
10. Dongosolo la non-tariff barrier reporting system.	28
11. Urongwa hwacho hunoshanda sei?	31


COMESA SIMPLIFIED TRADE REGIME (STR)



Zambia



Malawi



Zimbabwe

Kodi COMESA STR ndi chiyani kwenikweni?

Mukamva kuti Common Market for Eastern and Southern Africa (COMESA) STR amakhala akunena za dongosolo limene bungwe la COMESA linakhazikitsa popititsa patsogolo ntchito za malonda za anthu a mabizinesi aang'onoang'ono amene amagula ndi kugulitsa katundu wochepa chabe m'mayiko ena.



Abizinesi angathe kulowetsa ndi kutulutsa katundu wosapitirira \$2000, popanda kulipira msonkho uliwonse malingana ndi mgwirizano wa misonkho wa m'mayiko a COMESA.



Cholinga cha dongosolo limeneli ndicho kuchepetsa ndondomeko zoyenera kutsatiridwa kuti munthu atulutse kapena kulowetsa katundu m'mayikowa komanso ndicho kuchepetsa ndalama zimene abizinesi amalowetsa mu bizinesi yawo.



Dongosolo la COMESA STR layamba kale kugwira ntchito m'mayiko atatu a SADC; Malawi, Zambia, ndi Zimbabwe



Panaikidwa zinthu zinayi zothandiza kuti mfundo za m'dongosololi zizitsatiridwa; satifiketi yofotokoza mwachidule za komwe katundu akuchokera (Simplified Certificate of Origin), Fomu yofotokoza mwachidule za msonkho (Simplified Customs Document), mndondomeko wa katundu wodziwika bwino (Common List), ndiponso malire a mtengo wa katundu wogulitsidwa mu dongosololi (Threshold). Dongosolo la STR lilinso ndi munthu wotchewa TIDO (Trade Information Desk Officer) yemwe ntchito yake ndi kukuthandizani pa zomwe mukufunikira kudziwa.



Kodi muli ndi ziyeneretso zogwiritsa ntchito

Ziyeneretso zake ndi izi:

- Katundu amene muli naye analimidwa ndi kupangidwa m'mayiko a COMESA ndiye kuti ali mu ndondomeko ya STR
- Ngati katunduyo akagulitsidwe m'dziko limene mukupita loyandikana ndi dziko lanu (osati dziko limene mukungodutsamo)
- Ngati katunduyo sakupirira malire a mtengo wa katundu wololeka kutenga malingana ndi dongosolo la STR (US\$2000)
- Ngati katunduyo ali pa mndondomeko wa katundu wodziwika bwino wotchedwa Common List (simuyenera kulipira msonkho uliwonse pa katundu yense wa mndondomeko umenewu)
- Funsani TIDO kuti akusonyezeni mndondomekoku (Common List) ngati sanamate pepala la mndondomekoku pa bodapo kapena pa bolodi la chidziwitso la pafupi ndi pomwe mwaima
- Funsani TIDO kuti akusonyezeni mndondomekoku (Common List) ngati sanamate pepala la mndondomekoku pa bodapo kapena pa bolodi la chidziwitso la pafupi ndi pomwe mwaima

Kodi mndondomeko wa katundu wodziwika bwino (Common List) ndi chiyani?


Mndondomeko wa katundu wodziwika bwino ndi mndondomeko wa katundu amene mayiko awiri ogundizana malire anagwirizana kuti azidutsa m'maboda awo popanda kulipira msonkho malingana ndi dongosolo la COMESA STR.



Kodi pamafunikira kusainira mapepala ati kuti mugwiritsire ntchito dongosolo la COMESA STR?

Kuti mugwiritsire ntchito STR, muyenera kukhala ndi ma inivoyisi kapena kuti malisiti a katundu amene mukufuna kutuluka naye kapena kulowa naye m'dzikolo. Kuphatikiza apo, pamafunika zikalata za chilolezo kuti mutulutse kapena kulowetsa katundu winawake wokhudza zakumunda kapena zoweta.

Mukasonyeza satifiketi yofotokoza mwachidule za komwe katundu akuchokera (Simplified Certificate of Origin) ndiye kuti simulipira msonkho pa katundu wanu ndipo simupatsidwa malire aliwonse a mtengo wa katundu yemwe mukuloledwa kutenga, malingana ngati katundu wanuyo ali pa Common List ndipo mwamupereka pamodzi ndi satifiketiyo.



Malo Othandiza Zomwe Mukufunikira Kudziwa (Trade Information Desks)

Malo otchedwa Trade Information Desk aikidwa m'maboda osiyanasiyana mogwirizana ndi dongosolo la COMESA Simplified Trade Regime (STR) n'cholinga chothandiza komanso kudziwitsa anthu abizinesi zinthu zimene akufunikira podutsa maboda.



Pa malo a Trade Information Desk pamakhala Trade Information Desk Officer (TIDO) omwe amaikidwapo ndi timabungwe toona za malonda odutsa pa bodayo totchedwa Cross Border Traders Associations (CBTA) kapena mabungwe oimira timabungwe timeneti.

Cholinga cha TIDO ndicho kuthandiza abizinesi pa zomwe akufunikira zokhudza malonda awo ndiponso kuwadziwitsa zina ndi zina zokhudza katundu amene akulowetsa kapena kutulutsa, kuphatikizapo zikalata zonse zomwe akufunikira. Ngati angafunikirensa kutero, angathandizenso m'njira yomweyi abizinesi ena kayanso anthu kapena mabungwe amene amakhudzidwa ndi mabizinesi owoloka boda. Zimenezi zikuphatikiza kuti azikhala chikwanekwane kupeza zonse zokhudza nkhani izi (koma si zokhazi ayi):-

- Katundu amene anthu akugula ndi kugulitsa kwambiri
- Ziwerengero zosiyanasiyana zokhudza kuchuluka kwa anthu abizinesi amene akugwiritsira ntchito dongosolo la STR
- Nkhani zokhudza kuphwanya lamulo kapena kuchita nkhanza pochita zinthu ndi abizinesi amenewa monga pofuna kuti apereke ziphuphu kapena powazunza ndiponso zokhudza zinthu zomwe zimabwezera m'mbuyo abizinesi owoloka boda

- Zokhudza nthawi imene katundu ayenera kukhala pa boda asanalodwe kulowa kapena kutuluka m'dziko
- Kapezedwe ka zikalata kapena mapepala ofunikira komanso ngati aboma amene akugwira ntchito paboda akukwanitsa kuthandiza abizinesi onse pamene ayamba kuchuluka
- Kukonza malipoti a mwezi uliwonse kapena a pa miyezi itatu iliyonse ogwiritsidwa ntchito ndi a Cross Border Traders Associations (CBTA), COMESA ndiponso aboma;
- Kudziwitsa ena ntchito za CBTA
- Kupeza mitengo yoyenerera yogulitsira katundu amene abizinesi ambiri amanyamula.
- Kudziwitsa anthu dongosolo la misonkho ndiponso kusintha kulikonse pankhaniyi.
- Kudziwitsa abizinesiwa za malo ogona, mayendedwe, ndiponso zinthu zina zotere zomwe angafunikire paulendowo
- Kulangiza abizinesi pa nkhani zokhudza misonkho, zofunika kutsatira pa zamalonda ndiponso podutsa boda ndiponso polemba zofunika m'mafomu ndi mapepala ena a boma paboda.

Dongosolo lololezera katundu kulowa kapena kutuluka m'dziko

Abizinesi akafika pa boda amayenera kusanthula katundu wawo kuti katundu amene ali pa mndondomeko wa katundu wodziwika bwino (Common List) akhale payekha. Akatero, azitenga fomu yofotokoza mwachidule za msonkho ija, yotchedwa Simplified Customs Document, ndipo alembepe katundu wawo yense amene akupezeka pa mndondomeko wa Common List paja. Satifiketi yofotokoza mwachidule za komwe katundu akuchokera yotchedwa COMESA Simplified Certificate of Origin imayenera kusainidwa ndi kuikidwa chidindo ndi munthu woona za misonkho ya boma pa katundu wolowa m'dziko (customs).

Katundu amene amafunika chilolezo kuti alowe kapena kutuluka m'dziko kudzera mu dongosolo la COMESA STR

Katundu wotsatirayu amafunika chilolezo chochokera kwa amene ali ndi mphamvu zopereka chilolezo choterechi kuti mumulowetse kapenanso kumutulutsa m'dziko; Mankhwala, zakudya zakumunda, zinthu zochokera ku zomera kapenanso zoweta monga malalanje, nthochi mkaka, mankhwala ophera tizilombo, mazira, nsomba, nyama kapenanso nkuku.

Abizinesi ayenera kupeza chilolezo cholowetsa kapena kutulutsa katundu kuchokera ku Undunda wa Zaumoyo, Unduna wa Zaulimi ndiponso Bungwe Loyang'anira Zachilengedwe. Katundu amene amene angamulole kulowa kapena kutuluka m'dziko ndi katundu yekhayo amene akukwaniritsa ziyeneretso zonse zokhudza zinthu monga zakudya, zomera ndiponso nyama komanso ziyeneretso za kuteteza chilengedwe.

Kodi mungafunikebe kulipira msonkho wotchedwa VAT (Value-Added Tax) kapenanso wotchedwa Withholding Tax ngati muli ndi katundu wochepea?

Dongosolo la STR limagwira ntchito pa msonkho wolowetsera katundu m'dziko basi, motero m'mayiko ena, malingana ndi malamulo awo a msonkho, mungafunikirebe kulipira msonkho wa Value-added tax (VAT) excise duty ndiponso withholding Tax.


SITEPE 1 DUTSANI PA IMIGIRESHONI

Fikani pa ofesi ya imigireshoni ndi kudinditsa pasipoti yanu



SITEPE 2 LONGOSOLANI KATUNDU WANU

Ngati mukulowetsa katundu, musiyaniitsemi motere:
Ikani padera katundu okonzedwa m'chigawo cha COMESA yemwe ali pa ndondondomeko ya Common List amene simuyenera kulipirira msonkho ndipo mumusiyaniitse ndi katundu okonzedwa m'chigawo cha COMESA koma yemwe sali pa ndondomekoyi ndipo ayenera kulipiridwa msonkho.



SITEPE 3 SATIFIKETI YOTCHEDWA SIMPLIFIED CERTIFICATE OF ORIGIN

Lembani zofunikira pa COMESA Simplified Certificate of Origin, yomwe ndi satifiketi yofotokoza mwachidule za komwe katundu akuchokera. Satifiketiyo ikuyenera kusainidwa ndi kuikidwa chidindo ndi munthu wa Customs kuikira umboni za katundu amene ali pa Common List. MUSAYEREKEZE KUPEREKA NDALAMA kwa munthu wa Customs pa ntchito yake yolemba zofunika pa fomu imeneyi.



Ngati pa bodapo pali TIDO, angathe kukuthandizani kulemba mbali yanu ya zofunika kulemba pa fomuyo ndipo angathenso kukuyankhani mafunso ena amene mungakhale nawo.

KULOWETSA KAPENA KUTULUTSA KATUNDU POGWIRITSA NTCHITO DONGOSOLO LA COMESA STR

SITEPE 4 PEZANI CHILOLEZO PA KATUNDU WOKHUDZA ZAKUMUNDA KAPENA ZOWETA

Katengeni chilolezo kwa amene ali ndi mphamvu zopereka chilolezo choterechi ngati muli ndi katundu aliyense wofunika chilolezo monga wochokera ku zakumunda kapena ziweto.



SITEPE 5 KULIPIRA DUTY NDIPONSO VAT

Simulipira msonkho uliwonse wa a custom pa katundu amene ali pa ndondondomeko ya Common List komanso mungafunikirebe kulipira msonkho wa Excise duty ndiponso wa Value Added Tax (VAT) pa katunduyo.

Msonkho wa Customs Duty umasiyana ndi wa Excise Duty. Nthawi zambiri Excise Duty imalipiridwa pa katundu winawake monga zakumwa zam'botolo, mowa wamtundu wa kachasu, fodya, zophodaphoda, ndi katundu wina wotere wochechera m'mayiko ena.

Mukatero pitani kwa kashiya kuti mukalipire ngati pali msonkho wa Customs Duty, Excise Duty kapena VAT wofunika kulipira.

Mukamaliza zonse zofunikira, mudzavomerezedwa kumapita ndi katundu wanu

Ngati simukumvetsa penapake ndipo mukufunikira kumvetsa bwinobwino za COMESA STR yankhulani ndi TIDO pa malo a Trade Information Desk omwe ali pa boda kapenanso yankhulani ndi a ofesi ya customs ngakhalenso a Unduna woona za Malonda



Gulu 1: STR COMMON LIST (Katundu Wovomezedwa):

Ku Zambia ndi ku Malawi pamene bukuli limasindikizidwa

Dzina la Katundu	Nambala Yake ya HS
Mbuzi zamoyo	010420
Nkhosa zamoyo	010410
Akalulu amoyo	010690
Nsomba za fuleshi (nsomba zamoyo sizololeka)	030269
Nsomba zouma, zoyanika kapena zowamba	030569
Mkaka wa madzi, yogati ndi kilimu	040110 - 040130
Mbatata (komanso ya kachewere)	070110 - 070190
Soya	120100
Mtedza	120210 - 120220
Mpunga	100610 - 100640
Anyezi	070310
Nthochi	080300
Bowa (mumate mapepala osonyeza kumene bowayo analimidwa)	070951
Tomato	070200
Mbewu za mpendadzuwa (osati mbewu zokadzala)	120600
Nyenmba zouma (osati zokadzala)	071310 - 071390
Nandolo wouma (tchana)	071320
Masamba a tiyi	090230
Khofi	090111 - 090190
Shuga	170111
Zosemasema	442010 – 442090
Mipando ya nsungwi	940190
Zakudya za ziweto	230800, 230910
Juyisi	200912 - 200990
'Super Maheu (Thobwa woikamo zokometsera)	290690
Mabisiketi	190531

Dzina la Katundu	Nambala Yake ya HS
Nyama ya soya	21061090 – 23040000
Simenti	252329 – 252390
Laimu wa whaitiwoshi	252210



Gulu 2: STR COMMON LIST (Katundu Wovomezedwa):


Ku Zambia ndi ku Zimbabwe pamene bukuli limasindikizidwa.

Dzina la Katundu	Nambala Yake ya HS
Nyama zamoyo	0101 kusvika 0106
Mbatata (zaziwisi kapena zam'chitini)	0701
Tomato (wamuwisi kapena wam'chitini)	0702
Anyezi, galiki, mavwende	0703
Kabichi, kolifulawa, ndi zina zotere.	0704
Letesi	0705
Karoti, mpiru, tchomoliya, bitiruti, ndi zakudya zina zomera pansi	0706
Minkhaka, mphonda	0707
Nsawawa, nyemba ndi zina zokhala ngati nyemba (zaziwisi kapena zam'chitini)	0708
Ndiwo zina za masamba (asiparagasi, mabilinganya, celery, bowa, ndi zina zotere)	0709
Ndiwo zoyanika (Monga bowa osiyanasiyana ndi masamba)	0712
Nyemba zouma, nkhangudzu, mphodza (kuphakizapo mbewu yokadzala)	0713
Mbewu	0713
Nthochi	0803
Nkhuyu, zinanazi, mapeyala, magwafa, mango	0804
Malalanje, manachesi, zinyumwa, mandimu	0805
Mphesa (zaziwisi kapena zoyanika)	0806
Mapapaya	0807
Khofi (wokazinga/wosakazinga, wokhala ndi kafini/wopanda kafini)	0901
Tiyi (wa girini kapena wa bulaki)	0902
Mafuta a soya	1507
Mafuta a mtenda	1508
Mbewu ya mpendadzuwa, mafuta a thonje	1512
Mafuta ena ochokera ku zomera	1515

Dzina la Katundu	Nambala Yake ya HS
Majarini	1517
Shuga wochokera ku nzimbe kapena bitiruti	1701
Zakudya za shuga (kuphatikizapo chokoleti choyera ndi chingamu chosakhala ndi koko)	1704
Chokoleti ndiponso zakudya zina zotere zokhala ndi shuga	1808
Zakudya za ana akhanda zogulitsa mu golosale (kupatulapo mkaka wa ana monga Lactogen)	190110
Tomato (wokonzedwa kapena kusungidwa pogwiritsira ntchito viniga kapena acetic acid)	2002
Jamu wosiyanasiyana, mamaledi	2007
Pinati bata	200811
Juyisi	2009
Yisiti	2102
Supu	2104
Madzi (kuphatikizapo madzi am'botolo oikamo maminero kapena gasi, okhala ndi shuga kapena zotsemeretsa zina)	2202
Vinyo	2204
Whisike, ramu, jini, vodika, ndi zina zotere.	2208
Viniga	2209
Simenti	2523
Thonje	3005
Peni ndi vanishi (monga wopangidwa ndii: Astra, Chroma, Promac, Splash, Dulux and Prochem)	3208 - 3210
Inki wosindikizira, wolemba kapena wojambulira ndiponso wa mitundu ina	3215
Maperefyumu osiyanasiyana	3303
Mankhwala ophodera ndi opaka pakhungu	3304
Mankhwala a tsitsi	3305
Sopo	3401
Mankhwala otsukira	3402

Dzina la Katundu	Nambala Yake ya HS
Mapolishi ndi zopaka nsapato	3405
Mapaipi apulasitiki ogwiritsa ntchito pothirira	3917
Mapepala a pulasitiki ofolelera	392100
Masaka ndi matumba a pulasitiki	392321 - 392329
Mbale, mapoto, ndi zipangizo zina zotere ndiponso zinthu zina zapulasitiki zogwiritsidwa ntchito ku toileti (kuphatikiza zinthu za pulasitiki monga zitini za maluwa, makapu ndiponso mbale)	3924
Mathanki a pulasitiki a madzi	392510
Magulovu a pulasitiki	401511
Ma renikhoti a pulasitiki	401590
Matumba a zikwama zachikopa, ndi zina zotere.	4202
Zipangizo zosiyanasiyana zachikopa	4203
Matabwa odula ku fakitale	441011
Mawindo a matabwa, zitseko, nsanamira ndi mitanda, matabwa oyala pansu, ndi zina zotero.	4418
Zinthu monga madengu ndi mabasiketi	4602
Mapepala okulungiramo zinthu	4707
Mabuku olembapo, mabuku a mapepala olemba, kalata, mabuku a kusukulu, zosunga mapepala, mafoda, zikuto za ma faelo, ndi zina zotere.	4820
Pepala	4821
Mabuku osiyanasiyana ndiponso zinthu zina zosindikizidwa	4901
Zidoilo zoluka pamanja ndi zina zotere	5805
Zolukaluka (monga zongolekedwa penapake kapena zokongoletsera nsalu yonse)	5810
Zoyala pamwamba pa bedi	5811
Zopukutira monga matawelo osiyanasiyana	6001
Zovala zoluka	6002
Zovala (zatsopano zokha)	Chitsauko 61 ne62

Dzina la Katundu	Nambala Yake ya HS
Mabulangete ndi zovunda paulendo	6301
Nsalu zoyala pabedi, patebulo, ku toileti, ndiponso ku kutchini	6302
Nsapato zosalowa madzi	6401
Nsapatso za labala, pulasitiki, chikopa kapena zophatikiza chikopa ndi nsalu	6404
Magawo a nsapato	6405
Ma ekisitenshoni a tsitsi	6703
Mawaya ndiponso ma kebo a kopa	7408
Makina opangira 'Freezit'	833880
Makina opangira kandulo	841989
Mapulawo ndi zipangizo zake	843210 ne843290
Makina opangira pinati bata	843780
Mabatire a galimoto: Chloride, Victor onion, Exide	850710
Zipangizo za pa meni switchi ya magetsi (zokonzedwa ndi kampani monga Imperial komanso Mukonitonics)	853521-853529, 853620
Mashitchi	853530 ne853630 - 853650
Bopointi, zochekenera, ndi zina zotere.	9608
Ziboliboli kapena zosemasema zopezeka m'zipangizo zina	9703
Crisps	2005
Sopo wochapira wa 'STA-Soft'	3402
'Bisto' wothira munsuzi	2104
Ma padi a 'Nina'	5601
Maseti a masamu (Mathematical sets)	9017



Gulu 3: STR COMMON LIST (Katundu Wovomezedwa):

Ku Zimbabwe ndi ku Malawi pamene bukuli limasindikizidwa.

Dzina la Katundu	Nambala Yake ya HS
Nyama zamoyo	Kuphatikiza Chaputala 1 0101 kusvika 0106
Mazira aawisi a ndiwo kapena oti akaswe anapiye	0407
Mbatata (zaziwisi kapena zam'chitini)	0701
Tomato (wamuwisi kapena wam'chitini)	0702
Anyezi, galiki, mavwende	0703
Kabichi, kolifulawa, ndi zina zotere.	0704
Letesi	0705
Karoti, mpiru, tchomoliya, bitiruti, ndi zakudya zina zomera pansu	0706
Minkhaka, mphonda	0707
Nsawawa, nyemba ndi zina zokhala ngati nyemba (zaziwisi kapena zam'chitini)	0708
Ndiwo zina za masamba (asiparagasi, mabilinganya, celery, bowa, ndi zina zotere)	0709
Ndiwo zoyanika (Monga bowa osiyanasiyana ndi masamba)	0712
Nyemba zouma, khobwe, mphodza, kuphatikizapo za mbewu	0713
Mbewu	0713
Nthochi	0803



Gulu 4: STR COMMON LIST (Katundu Wovomezedwa)

Ku Malawi ndi ku Zambia pamene bukuli limasindikizidwa

Dzina la Katundu	Nambala Yake ya HS
Zakukhitchini (Mapoto a aluminiyamu ndi a chitsulo)	73.23 ne76.15
Ufa	11.02
Chimanga	10.05
Feteleza	31.05
Mbewu	Chitsauko 12
Zakudya zaziwisi monga nandolo, nyemba	07.08
Kabichi	07.04
Makaroti	07.06
Masamba	Chitsauko 7
Mango	08.04
Mtedza	12.02
Nyemba ndi nandolo wouma	07.13
Mazira	04.07
Thonje	23.03 23.06
Tsabola/paprika	09.04
Madzi a maminero/	22.01
Mafuta ophikira	15.12
Zipangizo zolowetsera mpweya m'nyumba	39.17
Matayelo a miyala	68.10
Nyemba zouma	07.13
Sopo ndi zotsukira zosiyanasiyana	34.01 34.02



Gulu 4: STR COMMON LIST (Katundu Wovomezedwa)

Ku Malawi ndi ku Zambia pamene bukuli limasindikizidwa

Dzina la Katundu	Nambala Yake ya HS
Zipangizo zapulasitiki zolowetsera mpweya m'nyumba	3917/3917.33
Saka lopanda kanthu	63.05
Chinangwa ndi zinthu zopangidwa kuchokera ku chinangwa	07.14 and 11.08
Zingwe za twaini	56.07
Mkaka wamadzi ndiponso zinthu zochoka ku mkaka	04.01
Zipangizo zopangira mipando ya nsungwi	56.07
Mbaula ndiponso dothi lopangira mbaula	68.15 and 25.08
Zoluka ndi manja (basiketi, treyi yoluka)	46.02
Mapira	10.08
Mapepala otengeramo zakudya	48.19
Tsabola wa m'botolo	21.03
Tishu	48.18
Mapepala opukutira m'manja patebulo	96.19
Mipando ya pulasitiki	94.03
Makandulo	34.06
Mapensulo	96.09
Zipangizo za aisi kilimu	21.05
Mapepala okulungiramo zinthu	47.07
Mashini opangira aisikilimu	8418.69.00
Mashini opangira popukoni	84.19 and 85.16
Zopangira faiba gilasi	39.26
Faiba gilasi	70.19
Mafelemu a m'ma windo	76.10
Ufa wa firigu	11.01
Zomatira m'mawindo	32.14
Thonje/mpendadzuwa/zamasamba/soyabean and groundnut oil	15.12,15.07 and 15.08

Dzina la Katundu	Nambala Yake ya HS
Masaka opanda kanthu	63.05
Zikopa	41.04 and 41.05
Zinthu zapulasitiki (makontena, beseni, mipando, mbale ndi makapu)	39.24, 39.26 and 94.03
Majarini	15.17
Mafuta odzola osiyanasiyana	33.04
Polishi wa m'nyumba komanso wansapato	34.05
Masiwiti, babogamu	17.04
Mabopeni ndi Mapensulo	96.08 and 96.09
Ulus wolukira	51.09
Makandulo	3406.00.0
Masinaki (chipisi cha m'pepala ndiponso kamba)	19.04 and 19.05
Penti	32.08 32.09
Makasu/Nkhwanga	82.01
Mabagi a pulasitiki	3923.21 3923.29
Mowa wa ngati kachasu	22.08, 22.06
Mapira	10.08
Matabwa a milongoti ya ku denga	92.06
Ng'oma	92.06
Makebo ndi mawaya magetsi	85.44
Zipangizo za nyimbo zamakolo	92.02
Mabelo a chikhalidwe ndiponso zipangizo zoimbidwa mogwiritsira ntchito miyendo	92.08
Zipangizo za Malimba Lozi instruments	92.02
Nyama yam'chitini kapena yam'pepala	16.02
Tchizi	04.06
Nsomba za fuleshi	03.04
Mowa wakuda	22.06
Zopondapo pakhomo	46.01

Dzina la Katundu	Nambala Yake ya HS
Zipangizo zokhudza ntchito zokonza za mapaipi	39.17
Chinangwa ndi zinthu zopangidwa kuchokera ku chinangwa	07.14 11.06
Malata	72.10
Zoyala patebulo za pulasitiki	39.26
Mawilibaala kapena galimoto	8716.80
Madiramu a pulasitiki	39.23
Mowa ukuluukulu	22.03



DONGOSOLO LA NON-TARIFF BARRIER REPORTING SYSTEM

Mabungwe a Common Market for Eastern and Southern Africa (COMESA) ndi Southern Africa Development Community (SADC) akhazikitsa njira yotumiza uthenga kudzera pa SMS Short Message Service(SMS) kuti azidziwitsidwa, zomwe zikubwezera m'mbuyo mabizinesi m'dera lino.

Mawu akuti Non-Tariff Barriers (NTBs) akunena za zinthu zomwe zimabwezera m'mbuyo abizinesi ndipo zimakhala chifukwa cha kuletsa zochita zina pa bizinesi, kuika malire pa katundu kapena ndalama, kapenanso malamulo enaake amene amachititsa kuti kulowetsa kapena kutulutsa katundu m'kuzikhala kovuta ndiponso koboola m'thumba.


Uthenga wa pa SMS umayendera limodzi ndi njira ina ya pa intaneti yokonzera ma lipoti, kuunika mmene zinthu zikuyendera ndiponso kuchotsa mfundo zimenezi za non-tariff barriers (NTB). Njira ya SMS iyamba kugwira ntchito monga mbali yolimbikitsa ndiponso kufulumizitsa ntchito yochotsa zopinga zonse zoterezi m'maboda.

Zitsanso za Zopinga Zolepheretsa Abizinesi Kupita Patsogolo

Kuletsa kulowetsa katundu m'dziko



Kuchulukitsa kapena kuchita tsankho pa nkhani ya malamulo a komwe katundu



Kuumirira kuti katundu wochokera m'dziko lina azikhala kwa kolite inayake



Kukhwimitsa kwambiri malamulo okhudza kuika katunduyo m'mapepala kapena m'zinthu zina zotere,




Kuona ngati dziko limene likutulutsa katunduyo lili ndi ziyeneretso,

Kukhwimitsa kwambiri malamulo okhudzau ukhondo komanso okhudza kulowetsa zinthu zakumunda,



Kulemba mawu odziwitsa anthu za katunduyo, kolite yake, ndipo za malamulo ambirimбири ofunikira,



Kuona ngati bungwe kapena kampani imene ikutumiza katunduyo kunja ili ndi ziyeneretso,

Kodi mukukumana ndi mavuto oterewa?

Kodi mukudziwa kuti mungathe kutumiza lipoti lofotokozero boma za mavuto amenewa pogwiritsa dongosolo la non-tariff barrier monitoring system?

Kodi mukukumana ndi mavuto potumiza kapena kulowetsa katundu wanu kuchoka m'dziko lina?

Perekani lipoti pogwiritsa ntchito manambala awa:

Zambia

SMS Namba:

+260976757643



Zimbabwe

SMS Namba:

+263715876373



Malawi

+265 992 595674



Eswatini

+27 72 949 2093



Mozambique

+27 72 949 2093



Sankhanipo dziko pa mndandanda wapamwambawu ndipo tumizani lipoti lanu ku NTB ndi mfundo zofunika:

- Kutikodi muli ndi vuto lotani?
- Linachitika liti ndiponso kuti?
- Dzina la wa bizinesi
- Nambala ya wa bizinesi

Urongwa hwacho hunoshanda sei?

1

Wodandaula amatumiza uthenga wake pa SMS kuti awadziwitsa za vuto lake

2

Uthenga ukusungidwa ku NTB ndipo munthu waudindo akudziwitsidwa

3

Iye akupereka ntchitoyi kwa a Regional Economic Community ndi a Focal Point m'deralo kuti athandizepo

4

Wodandaula akudziwitsidwa kuti dandaulo lake aliika m'manja mwa a Focal Point ndipo akulismalira

5

A m'gulu la Regional Economic Community ndi la Focal Points akuyamba kuchitapo kanthu pa vuto lija ndipo akulemba ndemanda zawo

6

Ngati vutolo atalikonza mkulu wolondoloza za mavuto amenewa amalemba pa compyuta kuti vutolo lakonzedwa

7

Wodandula uja amadziwitsidwa kuti dandaulo lake lija samaliridwa

☎ +27 11 318 1012

✉ info@southernafricatrust.org

🌐 www.southernafricatrust.org

📍 45 Kyalami Blvd, Kyalami Park,
Midrand, 1684, South Africa

